N’chifukwa Chiyani Mulungu Amalola Kuti Anthu Azivutika? (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m’mutu 11 wa buku lakuti, *Zimene Baibulo Limaphunzitsa* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI MULUNGU NDI AMENE AMACHITITSA KUTI TIZIVUTIKA?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N’chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti inde?

_____

N’chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti ayi?

_____

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

_____

_____

Nanga n’chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Yehova safuna kuti tizivutika.

(Werengani mutu 11 m'buku lakuti, *Zimene Baibulo Limaphunzitsa,* ndime 1 mpaka 5.)

Werengani 1 Petulo 5:7.

Kodi lembali likusonyeza bwanji kuti Yehova safuna kuti tizivutika?

Werengani Yobu 34:10.

Kodi Mulungu ndi amene amachititsa kuti tizivutika?



Kodi anthu amene anapanga galimoto angaimbidwe mlandu chifukwa choti munthu woyendetsa galimotoyo sakutsatira malamulo apamsewu? Mofanana ndi zimenezi, kodi n'zomveka kuimba Mulungu mlandu pa mavuto ochititsidwa ndi anthu?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Satana ndiponso zotsatira za kugalukira kwake n’zimene zimachititsa kuti tizivutika.

(Werengani mutu 11 m’buku lakuti, *Zimene Baibulo Limaphunzitsa,* ndime 6 mpaka 9.)

Werengani 1 Yohane 5:19; Chivumbulutso 12:9.

Kodi malembawa akusonyeza bwanji kuti ndi Satana amene amafuna kuti tizivutika?

Werengani Mlaliki 4:1; 8:9; 9:11.

Kuwonjezera pa zimene Mdyerekezi amachita, chinanso n’chiyani chimene chimachititsa kuti tizivutika?

Kodi kudziwa kuti Mulungu safuna kuti tizivutika komanso amatithandiza tikakumana ndi mavuto kumakuthandizani bwanji?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Mulungu ndi wankhanza. Amafuna kuti anthu azivutika.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri akhoza kuganiza choncho. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Popeza kuti dzikoli lili m’manja mwa Mulungu, ndiye kuti ndi iyeyo amene amafuna kuti zoipazi zizichitika.

MUNGANENE KUTI…

Zipembedzo zambiri zimaphunzitsa zimenezo. Koma ndimakhulupirira kuti Satana ndi amene akulamulira dzikoli chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania